Baibulo ya ana

Ikupasilani

Yesu Amachiritsa Wakhungu

Yolembedwa ndi: Edward Hughes

Yojambulidwa ndi: Janie Forest
Alastair Paterson

Yotengedwa ndi: Ruth Klassen

Yotathauzidwa ndi: Tapiwa Maraira

Yo pangidwa ndi: Bible for Children
www.M1914.org

©2022 Bible for Children, Inc.
Chilolezo: Muli ndi ufulu wotenga ndi kuchurukitsa makopewa koma osagulitsa.

Bartimeyu (bar-tim-ay-us) anali wakhungu, atakhala m'mphepete mwa msewu pafupi ndi Yeriko. Kupempha. Anthu ena achifundo ayenera kuti ankam'patsa kakobiri kapena kagawo kakang'ono ka chakudya pamene ankadutsa. Bartimeyu sakanatha kugwira ntchito chifukwa sankaona.



Iye akanakhoza kokha kupempha.

Tsiku lina, msewu waukulu unali wotanganidwa.
Bartimeyu adamva kuponda kwa mapazi ambiri.
Chinachake chachilendo chinali kuchitika.
Posakhalitsa munthu wakhunguyo adazindikira kuti chinali chiyani.

Yesu wa ku Nazarete anali mumzinda. Khamu la anthu linasonkhana kuti lione Yesu, kuti limve Iye.

“Yesu, Mwana wa Davide, mundichitire ine chifundo!” Chifukwa chiyani Bartimeyu analira? N’chifukwa chiyani ankaganiza kuti Yesu akhoza kumuthandiza? Mwina anamva za anthu ena amene Yesu anawachiritsa. Ena anali ogontha, ena osalankhula, ena opunduka – ndipo ena anali akhungu monga iyeyo.

“Mwana wa Davide, ndichitireni chifundo,” Bartimeyu anafuula mobwerezabwereza. Mawu ake anamveka ndi chiyembekezo.

Bartimeyu anali wotsimikiza pa chinthu chimodzi. Ngati sanalandire chithandizo tsopano, mwina sakanapezanso mwayi wina. Yesu mwina sadzadutsanso njira yake.

Bartimeyu adayenera kufikira Yesu. Koma anthu sanasunthe. “Sssshhh!” iwo anati. Anamuchenjeza kuti akhale chete.

Koma Bartimeyo sanatonthole.
Anapitiriza kukuwa. Mwadzidzidzi
Yesu anaima! Anamvetsera!
Analamula munthu wakhunguyo kuti
abwere naye kwa Iye! "Khala
wokondwa," anthuwo
anauza Bartimeyu.
"Nyamuka.
Akukuitana."

Atataya chofunda chake, Bartimeyu anadzuka nadza kwa Yesu.



“Ufuna kuti ndikuchitire chiyani?” Yesu anafunsa. Kodi mukanayankha bwanji? Kodi mukanapempha ndalama zambiri kapena zovala zabwino zatsopano? Kodi ndi zomwe Bartimeyu ankafuna?





Ayi, Bartimeyu wakhungu sanapemphe Yesu golide kapena zovala zabwino. Inu mukudziwa chimene iye ankafuna.

“Ambuye, kuti ndipenyenso.” Bartimeyo adafuna kuwona! Kuona mitengo ndi mbalame ndi kukongola konse kwa chilengedwe cha Mulungu. Ankafuna kuona kuti azitha kudzisamalira osati kukhala wopemphapempha.



Panepo Yesu anauza Bartimeyu kuti: “Yang'ana, chikhulupiro chako chakupulumusa.”



Pomwepo adapenyanso, namtsata Yesu. Zonse zimene ananena zinali “Mulungu ndi wodabwitsa! Anandichiritsa!” Inali nthawi yabwino kwambiri kwa Bartimeyo

Anthu onse, pakuona, analemekeza Mulungu. Apanso, anaona mphamvu yodabwitsa ya Mwana wa Mulungu, Yesu, yochititsa kuona munthu wosaona wosaona.

Yesu Amachiritsa Wakhungu

Nthano yochokera mu mau a Mulungu, Baibulo,

opezeka mu

Marko 10, Luka 18, Yohane 9

“Polowela pa mau anu pamapasa kuwala.”
Masalimo 119:130

Mapeto

Nthano iyi yamBaibulo imakamba za ubwino wa Mulungu yemwe anatipanga ndipo akufuna kuti mumdziwe iye.

Mulungu amadziwa kuti tima chita zoipa, zimene zimachedwa chimo. Chilango cha uchimo ndi infa, koma Mulungu anatikonda kwambiri ndipo anatuma mwana wake yekha, Yesu, kuzatifela pamtanda ndi kunzunzika chifukwa cha machimo anu. Ndipo anaukanso kwa akufa na pita kumwamba! Ngati ukukhulupirira Yesu mupempheni akukhululukileni machimo anu, azakukhululukirani! Adzabwera kukhala nanu, ndipo muzakhala naye kunthawi zonse.

Ngati mukukhulupirira kuti izi ndizoona, nenani ichi kwa Mulungu: Ambuye Yesu, ndikhulupirira ndinu mwana wa Mulungu, ndipo munakhala munthu kundifera ine machimo yanga, ndipo mulinso ndi moyo. Chonde, lowani mmoyo mwanga ndikundi khululukira machimo anga, kuti ndikhale ndi moyo watsopano, ndipo tsiku lina ndikakhale ndiinu muyaya. Ndithandizeni kukumverani ndi kukhala mwa inu ngati mwana wanu. Ameni.

Welenga Baibulo ndi kuyankula ndi Mulungu matsiku onse!
Johane 3:16